*Translation of the Customary*
*Land Act, 2016 and the Customary*
*Land Regulations, 2018*
*Author: Chikosa M. SILUNGWE, PhD*
*Assignment: FAO Gcp/Glo/347/MUL*
*26.08.19*
*Date of Finalization: 10.03.20*

# LAMULO LA MALO AMAKOLO, 2016

GAWO I – MAYAMBIDWE NDI KUGWIRITSA NTCHITO KWA LAMULO

**1.** Lamulo ili ndi Lamulo la Malo Amakolo, 2016.

GAWO II – KAYANG'ANIRIDWE KA MALO AMAKOLO

**2.** Malo amakolo ndi malo onse amene–

a) ali mudera lomwe limayang'aniridwa ndi Mfumu ya Ndodo;
b) malire ake anakhazikitsidwa ndi Komiti yoyang'anira malo amakolo ku dera-lo; kapena
c) ali ndi chiphaso choperekedwa ndi Mkulu woyang'anira za Malo mu Unduna wa za Malo.

**3.** (1) Chiphaso cha malo amakolo

a) chiperekedwe mu dzina la Mfumu ya Ndodo;
b) chimapereka mphamvu kwa Komiti yoyamg'anira za malo amakolo pakayendetsedwe ka malowo;
c) chimapereka umboni kuti anthu wonse amene ali pa malo amakolowo ndiwololedwa kukhala pamalowo motsatira mwambo waderalo.

(2) Mfumu ya Ndodo yili ndi udindo wosunga chiphaso cha dera lake mosamala.

(3) Malire a malo amene ali pansi pa ulamuliro wa Mfumu ya Ndodo sangasinthidwe popanda chilolezo cha Mkulu woyang'anira za malo ku Unduna wa za Malo.

(4) Mkulu woyang'anira za malo ku Unduna wa za Malo ali ndi udindo wosunga kalembera wa malo onse amene ali pa ulamuliro wa Mfumu ya Ndodo.

**4.** (1) Dera liri lonse la Gurupu lidzakhala ndi komiti yoyang'anira za malo.

(2) Komiti idzakhala ndi anthu awa–

a) Gurupu amene adzakhalenso wa pampando;
b) anthu ena asanu ndi mmodzi amene atatu mwa iwo adzakhala azimayi.

(3) Komiti idzayenera kukhala ndi chisankho ngati mmodzi wa mu Komiti–

a) wamwalira;
b) watula pansi udindo;
c) wamangidwa ndi abwalo la malamulo chifukwa chopezeka ndi mlandu wa chinyengo;
d) sangakwanitse kugwira ntchito ya Komiti chifukwa cha vuto lina liri lonse.

**5.** Komiti ya malo amakolo ili ndi udindo woyang'anira malo a makolo amene ali pa ulamuliro wa Gurupu.

**6.** Komiti ya malo amakolo ili ndi mphamvu yopereka chiphaso cha pa malo a makolo.

**7.** Chiphaso cha pa malo amakolo chidzaperekedwa mogwirizana ndi Mfumu ya Ndodo.

**8.** Mkulu woyang'anira za malo a ku Unduna wa za Malo adzapereka uphungu wakayang'anidwe ka malo.

**9.** (1) Dera liri lonse la Mfumu ya Ndodo lidzakhala ndi kalaliki amene adzakhelenso mlembi wa komiti yoyang'anira malo m'deralo.

(2) Kalaliki adzakhala nawo mu mndandanda wa anthu ogwira ntchito ku khonsolo ndipo ayenera kukhala ndi–

a) setifiketi ya Folomu Folo;
b) maphunziro akayang'anaridwe ka malo;
c) luso lowerenga mapu;
d) luso lakayezedwe ka malo;
e) luso lolemba mapu a m'dera la Mfumu ya Ndodo;
f) luso la kasungidwe ka kawundula wa kugulitsa kwa malo m'dera la Mfumu ya Ndodo;
g) uphungu wopereka kwa Komiti ya malo;
h) luntha lowonetsetsa kuti Malamulo a za Malo akutsatidwa.

**10.** (1) Komiti ili ndi mphamvu yoweruza mikangano ya malo.
(2) Mkulu wa Malo mu Unduna wa za Malo ali ndi mphamvu yoweruza mikangano ya milandu ngati a Komiti alephera.

**11.** Komiti ya malo siyoloredwa kupereka chiphaso pa malo amene ali–

a) odyetsera ziweto;
b) manda; kapena
c) wogwiritsidwa ntchito ndi mudzi wonse.

**12.** Ma lizi wonse amene adaperekedwa Lamulo-li lisadakhatsikidwe adzapitilira kukhala ma lizi wovomerezeka pa Malamulo a dziko lino.

**13.** (1) Munthu wa Komiti ya malo sayenera kutenga mbali pa nkhani imene ikhudza munthu wa ku banja lake.

(2) Anthu a ku banja la munthu wa Komiti ndi awa–

a) bambo ake;
b) mayi ake;
c) mwana wake;
d) mkazi kapena mwamuna wake;
e) mchimwene wake; kapena
f) mchemwali wake.

GAWO III – KUSINTHA KWA MALO AMENE NDI A'BOMA

**14.** (1) Nduna ya za Malo ili ndi mphamvu yosintha malo amene ali a'Boma ndikukhala malo amakolo.

(2) Nduna ya Boma-yi idzagwiritsa ntchito mphamvu zimene zili pa ndime (1) mowunikiridwa ndi Lamulo la Malo, 2016.

GAWO IV – CHITUKUKO CHA DZIKO NDI MALO OSAYENERA KUKHALA

**15.** (1) Nduna ya za Malo ili ndi mphamvu yopereka malo amene ali m'dera la Mfumu ya Ndodo ku Boma ngati malowo akufunika kuchitirapo chitukuko cha dziko.

(2) Nduna idzapereka chidzwitso chimene chidzanene izi–

a) dera lomwe malo aliri;
b) mulingo wa malo operekedwa ku Boma;
c) zolinga zoperekera malowo;
d) tsiku losachepera masiku makumi asani ndi anayi (90), limene malo azakhale a Boma.

(3) Komiti ya malo idzadziwitsa munthu aliyense amene anali ndi umwini wa malo amene aperekedwe ku Boma, kuperekedwa kwa malo-wo.

(4) Munthu amene ali ndi umwini wa malo amene aperekedwe ku Boma ali ndi ufulu kukapereka maganizo ake kwa Mkulu wa Malo ku Unduna wa za Malo.

(5) Mkulu wa Malo ku Unduna wa za Malo adzafotokozera a Komiti ndi anthu a m'dera la Mfumu ya Ndodo zifukwa zomwe malo am'deralo aperekedwere ku Boma.

(6) Malo adzaperekedwa ku Boma pokhapokha anthu amene atengeredwa malowo alandira chipukuta misozi.

(7) Bwalo lalikulu loweruza milandu la High Court lidzaweruza milandu yonse ya kusagwirizana pakaperekedwe ka chipukuta misozi.

(8) Nduna ya za Malo ili ndi mphamvu yolamula kuti bungwe limene likufuna, kapena munthu amene akufuna, lizi ayenera kupereka chipukuta misozi.

**16.** (1) Nduna ya za Malo ili ndi mphamvu yolamula kuti malo amene ali m'dera la Mfumu ya Ndodo siwoyenera anthu akhaleko.

(2) Khonsolo ili ndi mphamvu yopereka uphungu kwa Nduna wowunikira kwa Ndunayo malo a m'mudzi uli wonse amene siwoyenera anthu akhaleko.

(3) Malo amene siwoyenera anthu akhaleko ndi awa–

a) zithaphwi;
b) madambo kapena zilumba;
c) malo amene akuyenera kukhala ntaya wa zinyalala kapena zinyatsi;

d) malo amene ali ochepera ma mitala makumi asani ndi imodzi (60) kuchokera ku mtsinje kapena gombe la nyanja;
e) malo oletsedwa malingana ndi kafuku-fuku wa sayansi;
f) malo amene ali pachiwopsezo chodilizika;
g) malo amene ali ndi chilengedwe chofunika kutetezedwa.

(4) Anthu amene, kapena khonsolo imene, yakhudzidwa ndi chidziwitso adzapatsidwa chidziwitsocho.

(5) Chidziwitso chidzayikidwa pa malo onse owoneka m'dera lomwe anduna akufuna kupereka chigamulo choletsa kukhala ku malo-wo.

(6) Anthu onse amene adzalandire chidziwitso ali ufulu woyankhapo.

(7) Nduna ya za Malo idzadziwitse Pulezidenti nkhani ya malo amene anthu sakuyenera kukhalapo ngati pa malo-po pali lizi kapena chiphaso cha malo a-makolo.

(8) Chidziwitso cha malo osayenera kukhalachi chidzakhala ndi mphamvu ya Lamulo pamapeto pa masiku makumi atatu (30) kuchokera pa tsiku loyamba lopereka chidziwitsochi.

GAWO V – CHIPHASO CHA MALO AMAKOLO

**17.** (1) Chiphaso cha malo amakolo chili ndi mphamvu yofanana ndi lizi.

(2) Chiphaso cha malo amakolo chiperekedwe kwa–

a) m'badwa;
b) banja la m'badwa;
c) gulu la m'badwa;
d) kampani imene umwini wake ochuluka ndi m'badwa.

(3) Chiphaso cha malo amakolo–

a) chiyendetsedwe motsatira mwambo waderalo;
b) nchamuyaya;
c) chitha kuperekedwa pa wilo;
d) chitha kukhala ndi mfundo zowunikira kuchokera ku Komiti ya malo;
e) chitha kufufutidwa ndi Boma pamene Bomalo lapereka chipukuta misozi.

**18.** (1) Munthu kapena banja la m'badwa ayenera kupempha ku Komiti ya malo akafuna chiphaso cha malo.

(2) Komiti yili ndi mphamvu yoyitanitsa nkhani ina iliyonse pamene ikuwunikira pempho la chiphaso.

**19.** (1) Komiti iyenera kupereka chigamulo chopereka kapena kukaniza chiphaso pamasiku osadutsa makumi asanu ndi anayi (90).

(2) Popereka chiphaso, Komiti idzatsata–

a) chigamulo cha malire;
b) uphungu wa Mkulu wa malo ku Unduna wa za Malo;
c) fundo zokomera amayi pa umwini wa malo;
d) fundo zokomera anthu amene alibe malo ngati munthu akupempha chiphaso ndi mwana wa mmudzi amene ali ndi malo kale;
e) mulingo ndi zomwe zikufunikira pamalopo ngati wopempha ali wobwera;
f) fundo zokomera wopemphayo ngati munthu akukhala kale pamalopo.

(3) Komiti idzatsata uphungu wa Mkulu wa Malo ku Unduna wa za Malo ngati wopempha chiphaso ali bungwe.

(4) Komiti ili ndi mphamvu yopereka kapena kukaniza chiphaso.

(5) Komiti iyenera kulemba zifukwa zimene yakanira kupereka chiphaso.

**20.** (1) Komiti ya malo idzadziwitsa wopempha chiphaso cha malo malo amakolo polemba kalamba kalata ngati wopemphayo wapatsidwa chiphasocho.

(2) Wapampando ndi Mlembi wa Komiti ndi amene adzasayinire kalata yopita kwa wopempha chiphaso.

(3) Munthu amene anapempha chiphaso ali ndi ufulu wovomera kapena kukana kupatsidwa chiphasocho.

(4) Chiphaso chidzakhala chovomerezeka msonkho wa Boma ukaperekedwa.

**21.** Bungwe liyenera kupereka lendi ya pa chaka pamalo amene ali ndi chiphaso cha malo amakolo.

**22.** Komiti, mogwirizana ndi Mfumu ya Ndodo, adzayenera kuvomereza kugulitsa kwa malo amakolo mu zaka zoyamba zisanu kuchokera pa tsiku limene chiphaso chaperekedwa.

**23.** Malo amene ali ndi chiphaso cha malo amakolo ayenera kubwerera ku banja osati kwa munthu wadera pamapeto pa chiphaso.

**24.** Anthu awa ndiwoyenera kufunsidwa ngati afune umwini wa malo a chiphaso cha malo amakolo–

a) mkazi wa mwini chiphaso;
b) mwamuna wa mwini chiphaso;
c) ana a mwini chiphaso amene ndi a zaka 18 kapena kuposera.

**25.** Nduna ili ndi mphamvu yothetsa chiphaso cha malo amakolo.

**26.** Malo olekeleredwa koma pali chiphaso ndi amene–

a) sanalimidwe kwa zaka zosachepera zisanu zotsatana;
b) mwini malowo adatchona kunja kwa dziko ndipo palibe akuyang'anira malowo.

GAWO VI – NDONDOMEKO YA UMWINI

**27.** Chiphaso chidzaperekedwa kwa munthu kapena bungwe kulingana ndi malo amene ndondomeko ya umwini yatsatidwa.

**28.** Ndondomeko ya umwini idzatsatidwanso pamalo oyandikana ndi malo amene chiphaso cha malo chapemphedwa.

**30.** Ndondomeko ya umwini idzachitika–

a) dera la Mfumu ya Ndodo;
b) mu boma lonse.

**31.** Komiti ya malo ili ndi udindo woyendetsa ndondomeko ya umwini m'dera la Gurupu.

**32.** Khonsolo ili ndi udindo woyendetsa ndondomeko ya umwini mu boma lonse.

**33.** Khonsolo idzayimika ndondomeko ya umwini ngati anthu makumi awiri adandaula kuti ndondomekoyo siyikuyenda bwino.

**34.** Khonsolo ili ndi mphamvu yolamula Komiti ya malo kuti isinthe mokomera anthu wonse machitidwe a ndondomeko ya umwini wa malo.

**35.** Khonsolo, mwayonkha kapena mopemphedwa ndi anthu makumi asanu (50), ili ndi mphamvu yochita ndondomeko ya umwini pamalo amene chiphaso cha malo amakolo chapemphedwa.

**36.** Mfumu ya Ndodo iyenera kudziwitsa ma Komiti a m'dera lake pamene ndondomeko ya umwini yikuti iyambe.

**37.** Chidziwitso cha ndondomeko ya umwini chiyikidwe m'dera lomwe ndondomekoyo ichitike ndipo inene–

a) mulingo wa malo;
b) anthu onse amene akuti ndi eni malo;
c) anthu onse amene akukhala pamalopo.

**38.** Munthu amene sanakhutire ndi ndondomeko ya umwini ali ndi ufulu kukasuma ku Bwalo la milandu ya Malo limene wapampando wake ndi Mfumu ya Ndodo pasanathe masiku makumi atatu (30) chimalizireni ndondomekoyo.

**39.** Bwalo la aMfumu liri ndi mphamvu yosintha chigamulo cha ndondomeko ya umwini.

**40.** Munthu amene sanakhutire ndi chigamulo cha Bwalo la aMfumu ali ndi ufulu kukasuma ku Bwalo lomwe wa pampando ndi Bwana Mkubwa.

**41.** Ndondomeko ya umwini idzatsata mfundo izi–

a) umwini uyenera kuperekedwa kwa munthu amene wakhala pamalo zaka khumi ndi ziwiri (12) popanda wina kudzamufunsa za umwini wa malowo;
b) chikalata chachilolezo chokhalira pamalopo chilipo;
c) bungwe kapena kampani lakhala pamalopo ngati pa lendi;
d) malo opanda mwini adzakhala malo owetera ziweto;

e) malo amene amayerekezedwa kuti ndi a-makolo adzakhala malo a-Boma.

**42.** Fundo za ndondomeko ya umwini ziyenera kuwunikira ufulu wa amayi, achikulire, achilema ndi ana.

GAWO VII – KAWERUZIDWE KA MIKANGANO YA MALO

**43.** Mikangano ya malo yidzaweruzidwa motere–

a) Bwalo loyamba ndi Komiti ya malo;
b) Bwalo lachiwiri lomwe limaweruza milandu yochoka ku Komiti ndi Bwalo la Mfumu ya Ndodo;
c) Bwalo lachitatu lomwe limaweruza milandu yochoka kwa Mfumu ya Ndodo ndi Bwalo la Bwana Mkubwa;
d) Bwalo lachinayi lomwe limaweruza milandu yochka ku Bwalo la Bwana Mkubwa ndi Bwalo lomwe wapampando ndi Majesitereti.

**44.** (1) Bwalo la Mfumu ya Ndodo lidzakhala ndi anthu awa–

a) Mfumu ya Ndodo womwe ndi wa pampando;
b) Anthu wena asanu ndi mmmodzi omwe atatu mwa iwo ndi azimayi.

(2) Anthu a Bwalo la Mfumu ya Ndodo ayenera–

a) kudziwa mwambo wa ku deralo;
b) kukhala akachenjede pa nkhani za mmudzi;
c) kukhala wolemekezedwa mmudzi.

(3) Munthu siwoyenera kukhala mu Bwalo la Mfumu ya Ndodo ngati ali–

a) mu Komiti ya malo;
b) mulendo ku deralo;

c) mphungu wa Nyumba ya Malamulo;
d) Majisitereti;
e) Ndi zaka zochepera 18;
f) Wamisala;
g) Womangidwapo pa mlandu wachinyengo;
h) Woti si'm'badwa.

(4) Munthu atha kukhala mu Bwalo la Mfumu ya Ndodo kwa zaka zitatu.

(5) Munthu ali ndi ufulu kukasuma ku Bwalo la Bwana Mkubwa ngati sanakhutire ndi chigamulo cha Bwalo la Mfumu ya Ndodo.

**45.** (1) Anthu awa adzakhala mu Bwalo la Bwana Mkubwa–

a) Mafumu a Ndodo atatu;
b) Anthu atatu awulemu wawo m'deralo amene awiri ayiwo adzakhala azimayi;
c) Mlembi wa za malo wa Bomalo.

(2) Khonsolo ili ndi mphamvu yosankha anthu a Bwalo la Bwana Mkubwa.

(3) Munthu ali ufulu kukasuma ku Bwalo la Majisitereti ngati sanakhutire ndi chigamulo cha Bwalo la Bwana Mkubwa.

**46.** (1) Anthu awa adzakhala mu Bwalo la Majisitereti–

a) Majisitereti yemwenso ndi wa pampando;
b) Mafumu a Ndodo atatu;
c) Anthu ena awiri awulemu wawo m'bomamo.

(2) Mkulu wa Malo mu Unduna wa za Malo mogwirizana ndi Mkulu wa ma Jaji wonse ndi amene ali ndi mphamvu yosakha anthu amene adzakhala pa Bwalo la Majisitereti.

**47.** Woweruza mikangano ya malo adzatsatira fundo izi–

a) Ufulu wa anthu wonse wokhudziwa ndi mlandu;
b) Malamulo wonse a Dziko kuyambira Konsitichushoni, malamulo opangidwa ku Nyumba ya Malamulo ndi miyambo ya dziko;
c) Zonse zomwe zingawunukire kaweruzidwe kachangu ka mikangano.

## GAWO VIII - ZOWONJEZERA

**48.** Lamulo ili silikuvomereza chiphaso cha malo kapena kugulitsana kwa malo kumene kunachitika mnjira ya chiphuphu.

# LAMULO LOTHANDIZIRA LAMULO LA MALO AMAKOLO, 2018

POGWIRITSA ntchito mphamvu zimene zili pa Ndime 53 ya Lamulo la Malo amakolo, 2016, Ine, ANNA ANDREW NAMATHANGA KACHIKHO, Nduna ya Boma yoyang'anira za Malo, ndakhazikitsa lamulo ili—

GAWO I

MAYAMBIDWE

**1.** Ili ndi Lamulo la mchaka cha 2018 lomwe ndi lothandizira Lamulo La Malo amakolo, 2016.

GAWO II

MA-KOMITI A MALO AMAKOLO

**2.** Kalaliki wa mdera la Mfumu ya Ndodo—

(a) apereke chidziwitso kwa a Gurupu choyitanitsa mayina a anthu wonse a mdera la a Gurupuwo amene ali ndi zaka khumi ndi zisanu ndi zitatu (18) kapena kuposera;

(b) ayitanitse mayina a anthu a mdera la nyakwawa-yo amene ali ndi zaka khumi ndi zisanu ndi zitatu (18) amene afune kuyimira chisankho cha Komiti;

(c) Adzalandira mayina a anthu wonse amene akufuna kuyima pa chisankho-cho osachepera masiku makumi awiri ndi limodzi (21).

**3.** Munthu ali woyenerezedwa kukhala mu Komiti ngati—

(a) ali m'badwa;
(b) ali mzika ya mderalo;
(c) ali ndi zaka khumi ndi zisanu ndi zitatu (18);
(d) sali Phungu wa ku Nyumba ya Malamulo;
(e) sali Khansala;
(f) sali Jaji kapena Majisitereti;

(g) sagwira ntchito m'boma;
(h) alibe udindo ku chipani cha ndale;
(i) alibe misala;
(j) sadamangidwepo pa mlandu wa chinyengo.

**4.** Munthu ayenera kutula pansi udindo wa m'Komiti ngati—

(a) alephera kugwira ntchito ya Komiti chifukwa cha chilema;
(b) Bwalo la Milandu lidagamula kuti alibe chuma chili chonse;
(c) asankhidwa u Khansala;
(d) asankhidwa u Phungu wa ku Nyumba ya Malamulo; kapena
(e) anamagidwapo pa mlandu wa chinyengo.

**5.** (1) Kalaliki adzapereka chidziwitso cha chisankho pamene anthu a M'Komiti aperewedwa.

(2) Zokambirana za Komiti zidzikhala zopanda pake chifukwa chakuti Komiti inaperewedwa pa nthawi ya zokambirana-yo.

**6.** (1) Komiti ili ndi mphamvu yophatikizira anthu atatu, mmodzi mwa iwo akhale mzimayi, chifukwa cha ukatswiri wawo.

(2) Anthu amene Komiti yaphatikizira alibe mphamvu yoponya nawo voti pa msonkhano wa Komitiyo.

(3) Munthu amene angaphatikiziridwe mu Komiti ayanera kukwaniritsa Ndime 3.

**7.** Munthu ayanerezedwe kuponya nawo voti ya chisankho cha Komiti ngati—

(a) ali m'badwa;
(b) ali ndi zaka khumi zisanu ndi zitatu kapena kuposera (18);
(c) ndi mzika ya mderalo;
(d) adalembetsa kwa a Gurupu a mukawundula wa anthu oponya voti.

**8.** Kalaliki adzayendetsa chisankho polengeza anthu amene akupikisana ndiponso powonesetsa kuti anthu aponya voti yawo mwa chinsisi.

**9**. Komiti igwire ntchito izi—

(a) kuwunikira eni malo ndi kagwiritsidwe ntchito ka malo mdera la a Gurupu;

(b) kuwonetsetsa kuti malire a malo wonse ndiwodziwika;

(c) kuyendetsa ndondomeko ya umwini wa malo;

(d) kugawa ziphaso za malo amakolo mogwirizana ndi Mfumu ya Ndodo;

(e) kuyeza mulingo wa malo amene angaperekedwe kwa munthu kapena bungwe;

(f) kulumikizana ndi mabungwe ogwira ntchito za malo, nkhalango, ulimi ndi chitukuko cha mdera la a Gurupu;

(g) kutolera msonkho wa malo;

(h) kuyendera ndi kutsimikiza ngati Ndondomeko zopelekera malo a makolo zatsatidwa;

(i) kuvomereza malonda a malo amakolo kwa zaka zisanu zoyamba chiperekereni chiphaso cha malo amakolo;

(j) kuphunzitsa anthu a mdera la a Gurupu mfundo za Lamulo la Malo amakolo;

(k) kupereka uphungu kwa Khonsolo pakalembedwe ka anthu a ntchito ya za malo.

**10.**—(1) Komiti ikumane kamodzi pa mwezi.

(2) Wapampando ayitanitse msonkhano wa Komiti.

(3) Mopemphedwa ndi anthu atatu a m'Komiti, Wapampando wa Komiti ayitanitse msonkhano wapadera posapitilira masiku khumi ndi anayi (14) chilandilireni pempholo.

(4) Komiti idzasankha mmodzi mwa iwo wapampando wogwirizira ngati Wapampando sanakwanitse kukhala nawo pa msonkhano-wo.

**11.** Kalaliki apereke chidziwitso cha msonkhano wa Komiti koma chidziwitsochi chisachepere masiku asanu ndi awiri kufikira tsiku la msonkhano.

**12.** Msonkhano wina wuli wonse wa Komiti udzapitilira ngati pali Wapampando ndi anthu ena atatu, amene awiri mwa iwo ndi azimayi.

**13.** Chigamulo cha Komiti chidzatengera voti ya anthu a m'Komiti.

**14.** Kalaliki, ngati mlembi, adzasunga makalata azokambilana zonse za Komiti.

## GAWO III
## NDONDOMEKO YA UMWINI

**15.** Komiti, mogwiritsa ntchito ulangizi wa akulu-akulu woyang'anira za Malo ku Unduna wa za Malo, idzachititsa misonkhano yowunikira kagwiritsidwe ntchito ka bwino ka malo amakolo.

**16.** Khonsolo idzapereka umboni wa malire a malo kwa Mlembi wa za Malo pa boma ndipo malire amenewa ndi a malo a kwa a Gurupu, Mfumu ya Ndodo ndi boma lonse.

**17.** Mlembi wa za malo adzayang'anira ndondomeko ya umwini wa malo ndi kukonza mapu a malo pa boma.

**18.** Mlembi wa za Malo adzasindikiza mapu a malo a Mfumu ya Ndodo ndi a Gurupu wosonyeza malire a malo mmaderawo.

**19.** Kalaliki, mogwirizana ndi Komiti, adzatsimikizira malire a malo potsatira mapu osindikizidwa mwa mphamvu ya pa Ndime 17.

**20.**—(1) Kalaliki adzapereka chidziwitso chosachepera masiku asanu ndi awiri chodziwitsa anthu Ndondomeko ya umwini wa malo.

(2) Chidziwitso chiyikidwe pamalo wowonekera kuti anthu ambiri achiwone ndi kuwerenga.

**21.** Munthu adziwitse, kapena bungwe lidziwitse, Kalaliki malire a malo pa nthawi ya Ndondomeko ya umwini.

**22.** Kalaliki agwire ntchito izi—

(a) kutsimikizira malire a malo ndi eni malo;
(b) kujambula mapu a malo;
(c) kusungira njira ndi malo ena onse wogwiritsidwa ndi gulu;
(d) kupereka malangizo pa nkhani za malo motsatira mwambo wa mdera-lo;
(e) kuwonetsetsa kuti mboni zilipo pa ndondomeko ya umwini;
(f) kuteteza Ufulu wa anthu kulibe pa ndondomeko ya umwini, azimayi, ana, wokalamba ndi achilema;
(g) kugamula mikangano ya malo;
(h) kupereka nambala ya malo ali wonse mdera la nyakwawa.

**23.** (1) Kalaliki apereke chidziwitso chosachepera masiku makumi atatu (30) kwa anthu amene adzafune kuwunikira kawundura wa Ndondomeko ya umwini.

(2) Kalaliki adzasunga kawundulayi kwa masiku makumi asanu ndi limodzi (60).

**24.** Chidziwitso choperekedwa pa Ndime 23 chidzayikidwa malo wowonekera kuti anthu ambiri achiwone ndi kuwerenga.

**25.** Mikangano yokhudza malo idzagamulidwa potsata Gawo V.

**26.** Pamapeto pa mikangano yonse ya malo, Ndondomeko ndi mapu wonse adzalembedwa mu kawundula potsatira Gawo IV.

GAWO IV

CHIPHASO CHA MALO AMAKOLO

**27.** — (1) Kalembera wa chiphaso cha malo amakolo adzatsatira Ndondomeko ya umwini.

(2) Munthu akafuna kulembetsa chiphaso cha malo amakolo akuyenera alembe kalata ya Form A ku Komiti.

**28.** Komiti itsatire izi—

(a) iwonetsetse kuti palibe munthu wina amene ali mwini malo;
(b) malo-wo ndiwoyenera kugwiritsidwa ntchito yomwe yanenedwa;
(c) mulingo wa malo ndiwoyenera ndi ntchito yomwe yanenedwa;
(d) ziphaso zomwe ali nazo kale munthu akupempha chiphasoyo.

**29.** Komiti itsatse chiphaso molingana ndi kalata ya Form B.

**30.** Munthu amene amapempha chiphaso abwere ndi kalata ya Form C, ndipo Komiti idzapereka chiphaso ndi kalata ya Form D.

**31.** Komiti ili ndi mphamvu yosapereka chiphaso.

**32.** Kalaliki adzasunga kawundula wa malo wonse amene a Komiti analembera.

GAWO V

KAWERUZIDWE KA KUSAGWIRIZANA PA NKHANI YA MALO

**33.** Munthu amene sanakhutire ndi chigamulo cha Komiti assume kwa a Komiti.

**34.** (1) Komiti isankhe munthu, amene sali m'Komiti kuti agamule kusagwirizana.

(2) Munthu amene asankhidwe pa Ndime (1) pamwambapa akwaniritse Ndime 3.

**35.** Komiti, mogwirizana ndi mkhala pakati, apereke chidziwitso cha tsiku lokamvera kusagwirizana polemba kalata ya Form E.

**36.** Munthu amene sanakhutire ndi chigamulo cha mkhala pakati wa Komiti ali ndi ufulu kukasuma ku Bwalo la Mfumu ya Ndodo potsatira kalata ya Form F.

**37.** Munthu amene wasumilidwa ayenera kuyankha pogwiritsa ntchito kalata ya Form G.

**38.** Bwalo la Mfumu ya Ndodo lidzadziwitsa onse tsiku la mlandu pogwiritsa kalata ya Form E.

**39.** Bwalo la Mfumu ya Ndodo lidzawonetsetsa kuti mlandu uthe bwino ndipo ngati wodandaula ndi wodandaulidwa agwirizana, Bwalo lidzalemba kalata yofotokoza mgwirizano umene mbali ziwirizo zachita.

**40.** Bwalo la Mfumu ya Ndodo lidzagamula mlandu pomvetsera umboni ngati wodandaula ndi wodandaulidwa alephera kugwirizana.

**41.** Samani ya mboni yochoka ku Bwalo la Mfumu ilembedwe pa kalata ya Form H.

**42.** Bwalo lidzapereka chigamulo ngakhale makalata kapena mboni palibe.

**43.**Bwalo lidzapereka chigamulo pa masiku osadutsa makumi asanu ndi limodzi (60).

**44.** Munthu aliyense ali ndi ufulu womvetsera kusagwirizana ku Bwalo la Mfumu ya Ndodo.

**45.** Bwalo la Mfumu ya Ndodo liyenera kusunga kawundura motere—

(a) tsiku lolembetsa mkangano;
(b) nambala ya mkangano;
(c) dzina ndi kokhala wodandaula;
(d) dzina ndi kokhala wodandaulidwa;
(e) chidandaulo ndi chigamulo chimene chikufunika;
(f) dzina la membala aliyense wa Bwalo;
(g) chigamulo;
(h) tsiku la chigamulo.

**46.** Munthu amene sanakhutire ndi chigamulo cha Bwalo la Mfumu ali ndi ufulu wokasuma ku Bwalo la Bwana Mkubwa.

**47.** Bwalo la Bwana Mkubwa likuyenera kumvera mikangano pasanathe masiku makumi atatu chilandilireni chi samani cha wodandaula.

**48.** Bwalo la Bwana Mkubwa lipereke chidziwitso cha tsiku lokamvera mkangano polemba kalata ya Form E.

**49.** Bwalo la Bwana Mkubwa lidzagamula mlandu pomvetsera umboni ngati wodandaula ndi wodandaulidwa alephera kugwirizana.

**50.** Samani ya mboni yochoka ku Bwalo la Bwana Mkubwa ilembedwe pa kalata ya Form H.

**51.** Bwalo la Bwana Mkubwa lidzapereka chigamulo ngakhale makalata kapena mboni palibe.

**52.** Bwalo la Bwana Mkubwa lidzapereka chigamulo pa masiku osadutsa makumi asanu ndi limodzi (60).

**53.** Munthu aliyense ali ndi ufulu womvetsera mkangano ku Bwalo la Bwana Mkubwa.

**54.** Munthu amene sanakhutire ndi chigamulo cha Bwalo la Bwana Mkubwa ali ndi ufulu kukasuma ku Bwalo la Majisitereti.

**55.**Bwalo la Majisitereti lidzapereka chigamulo pa masiku osadutsa makumi asanu ndi limodzi (60).

**56.** Munthu amene sanakhutire ndi chigamulo cha Bwalo la Majisitereti ali ndi ufulu kukasuma ku High Court.

## GAWO VI
## CHIPUKUTA MISOZI

**57.** Munthu alandire chipukuta misozi motsatira Lamulo la chipukuta misozi pa nkhani za malo lomwe linakhazikitsidwa mchaka cha 2016.

FORM A

KUFUNSIRA CHIPHASO CHA MALO AMAKOLO

1. Dzina ndi pokhala: *[Mutha kuyikanso dzina la bizinesi yanu].*

   ………………………………………………………………………………………..

2. Muli pa banja?

   ………………………………………………………………………………………..

3. Muli ndi ana? Lembani mayina ndi zaka zawo

   …………………………………………………………………………………………
   …………………………………………………………………………………………
   …………………………………………………………………………………………
   …………………………………………………………………………………………

4. Ngati muli pa banja, chiphaso-chi mulembetsa ndi akubanja kwanu?

   …………………………………………………………………………………………

5. Dzina la bizinezi (*ngati ilipo*)
   ……………………………………………………………………………………………
6. Dzina la Wofunsira: ………………………………………………………………..

   Nambala ya u-Mzika:.……………………………………………………………………

7. Malo ali mdzina lanu pa Lizi

   …………………………………………………………………………………………
   …………………………………………………………………………………………
   …………………………………………………………………………………………

8. Ntchito ya malowo ndi chani?

   ………………………………………………………………………………………….
   ………………………………………………………………………………………….

9.
   *(a)* Dera lomwe kuli malowo:...……………………………………………………..
   *(b)* Mulingo wa malowo:…..………………...……………………………………………………
   *(c)* Nambala ya malowo:……………………………………………………………

Tsiku:……………………………………………………….20…

……………………………………..
[*Dzina la Wofunsira*]

FORM B

KUTSATSA MALO OFUNIKA CHIPHASO CHA MALO AMAKOLO

Kwa: ……………………………..
……………………………..

Komiti yaganizira pempho lanu la malo ofunika chiphaso cha malo amakolo.

Komiti ikukutsatsani malo ali Nambal…………………...

Kutsatsa-ku kwaganiziranso izi:

…………………………………………………………………………………………………
…………………………………………………………………………………………………
…………………………………………………………………………………………………
…………………………………………………………………………………………………
…………………………………………………………………………………………………

Tsiku:…………………… ……………………………, 20…

…………………………..                                                        …………………………

Wa-Pampando                                                        Kalaliki

*Muyenera kuvomera kutsatsa-ku pasanathe masiku makumi asanu ndi limodzi kuchokera tsiku lalembedwa pamwamba-pa

FORM C

KUVOMERA KUTSATSIDWA MALO OFUNIKA CHIPHASO CHA MALO AMAKOLO

Kwa: Wa-Pampando (*Tchulani dzina la Komiti*)

………………………………………..

………………………………………..

Ine, A.B., NDAVOMERA kutenga malo ofunika chiphaso cha malo amakolo omwe ali Nambala …………………………….

Tsiku:………………………………………, 20…

…………………………………………..

Wofunsira

---

FORM D

CHIPHASO CHA MALO AMAKOLO

Ndondomeko ya Umwini…………………………… Nambala. ………………………………

Uwu ndi UMBONI wotsimikizira kuti ......................................................................... ndi/ndiwo eni malo ali Nambala…………………….

Malowa aperekedwa potsata mfundo izi:
………………………………………………………………………………………………
………………………………………………………………………………………………
………………………………………………………………………………………………
………………………………………………………………………………………………
………………………………………………………………………………………………
………………………………………………………………………………………………

……………………..
*Mwini wa Malo*

……………………. *Wa-Pampando*
Komiti

……………………. *Kalaliki*

Tsiku:…………………………………………….., 20…

..................................................
Mlembi wa za Malo pa Boma

[Kumbuyo]

Chiphaso chatsatiranso mfundo izi—

(a) Malo asamalidwe potsatira mfundo za ulimi wamakono;
(b) Osamanga nyumba popanda chilolezo;
(c) Khomerani msonkho wa malo ngati kuli kofunikira kutero;
(d) Tsatirani Malamulo wonse a Komiti ya za malo;
(e) Samalirani malire a malo; ndi
(f) Mkulu wa za Malo mu Unduna wa za Malo ali ndi mphamvu yoyendera malo-wa.

FORM E

CHIDZIWITSO CHA TSIKU LOMVERA KUSAGWIRIZANA

Kusagwirizana Nambala. ……. ya 20…

PAKATI PA

……………………………………………………………………………… Wodandaula

NDI

…………………………………………………………………………..……Wodandaulidwa

Kwa: ………………………………….

……………………………………..

KUSAGWIRIZANA kwanu kukhala pa Bwalo tsiku la…………………………………….., 20… kuyambira nthawi ya …………………..[mmawa][masana] ku……………………………..

Ngati simudzafika ku Bwalo pa tsiku-li, chigamulo chidzatha kuperekedwa inu kulibe.

Tsiku:……………………………………………., 20…

…..……………………………………

Wa-Pampando

---

FORM F

KUSUMIRA KUSAGWIRIZANA

Kusagwirizana Nambala. …….ya 20…

PAKATI PA

……………………………………………………………………………… Wodandaula

NDI

………………………………………………………………………………Wodandaulidwa

Kwa: Wa-Pampando

Ine ndikusuma ku Bwalo la …………………………………. Kuti mundipatse chigamula cha kusagwirizana wa za malo—

1. Wodandaula:
   (a) Dzina:…………….. ……………………………………………….
   (b) Pokhala:……..………………..…………………………………….
   …….……………………………………………………………...…...
   (c) Nambala ya wu Mzika:…………………… …………………………

2. Wodandaulidwa:
   (a) Dzina: ……………………...…………………………………….
   (b) Pokhala:…………………..…………………………………………

……..…………………………………………………………...…...

(c) Nambala ya wu Mzika:…………………… …………………………

3. Tsatane-tsatane wa kusagwirizana:
…………………………………………………………………………………
…………………………………………………………………………………
…………………………………………………………………………………
…………………………………………………………………………………
…………………………………………………………………………………
…………………………………………………………………………………
…………………………………………………………………………………
…………………………………………………………………………………
…………………………………………………………………………………
…………………………………………………………………………………
…………………………………………………………………………………
…………………………………………………………………………………
…………………………………………………………………………………
…………………………………………………………………………………
…………………………………………………………………………………
…………………………………………………………………………………
…………………………………………………………………………………
…………………………………………………………………………………
…………………………………………………………………………………
…………………………………………………………………………………
…………………………………………………………………………………

4. Malo:

(a) Dera: ………………………………………………………………………………….

(b) Nambala: ………………………………………………………………………………….

(c) Mulingo: ……………………………………………...……………………………..

(d) Mwini malo:…. ……………………………………………………………..

……………………………………….

Wodandaula

FORM G

YANKHO LA KUSAGWIRIZANA

Kusagwirizana Nambala. …… ya 20…

PAKATI PA

……………………………………………………………………………… Wodandaula

NDI

………………………………………………………………………………Wodandaulidwa

Kwa: Wa-Pampando

Ine, ………………………………………., amene ndili Wodandaulidwa, Yankho langa liri motere:

…………………………………………………………………………………
…………………………………………………………………………………
…………………………………………………………………………………
…………………………………………………………………………………
…………………………………………………………………………………
…………………………………………………………………………………
…………………………………………………………………………………
…………………………………………………………………………………
…………………………………………………………………………………
…………………………………………………………………………………
…………………………………………………………………………………
…………………………………………………………………………………
…………………………………………………………………………………
…………………………………………………………………………………
…………………………………………………………………………………

……………………………………….

Wodandaulidwa

FORM H

SAMANI YA MBONI

Kusagwirizana Nambala. ….. ya 20…

PAKATI PA

………………………………………………………………………………… Wodandaula

NDI

…………………………………………………………………...……Wodandaulidwa

Kwa: ………………………………….

…………………………………......

MUYENERA kufika ku Bwalo la ………………………………. pa ………………………, 20… nthawi ya ………………. [mmawa] [masana] kuti mudzapereke UMBONI.

Tsiku:……………………………………………, 20…

……………………………………….

Wa-Pampando

MALIPIRO NDI DIPO

Gawo A

| | K |
|---|---|
| Kufinsira Chiphaso cha malo amakolo | 1,000 00 |
| Chiphaso cha malo amakolo | 1,000 00 |
| Kusuma ku Bwalo la Mfumu ya Ndodo | 2,000 00 |
| Kusuma ku Bwalo la Bwana Mkubwa | 5,000 00 |
| Kusuma kwa Majisitereti | 10,000 00 |

Gawo B

| | |
|---|---|
| Kuphwanya mfundo za Chiphaso cha Malo amakolo | 10,000 00 |

Tsiku la 7 March, 2018

ANNA A.N. KACHIKHO

(Fayilo Nambala yake. LHUD/C/1) *Nduna ya za Malo*